JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION

"Promoting Faith and Justice"

P.O. Box 37774

10101 Lusaka, Zambia

Tel: 260-1-290410 **fax: 260-1-290759**

E-mail: jctr@jesuits.org.zm **web: www.jctr.org.zm**

October 2OO6

Malonje kuchokera kuno JCTR!

Ndife okondwa pokutumizirani mlozo wa kagawidwe ka mau mu nyengo ya Adventi mu chaka cha 2006. Tikhuluphirira ndi kuyembekeza kuti za maphunziro aumunthu monga Eklezia Katolika aphunzitsira adzakuphindulirani ndikukuthandizani pa kagawidwe ka mau mu nyengo ino yonse ya Adventi. Tizindikira kuti mkhalidwe ndi utsogoleri wa mzimbumba uzagwiritsidwa nchito pakukometsa uwu mlozo.

Chakhala chotifika kuti anthu amagwiritsa ntchito mlozo wakagawidwe ka mau mumapemphero, ndi mumisonkhano ya muma mbumba, mu misonkhano ya anyamata ndi atsikana ndi mapemphero ena ake.

Nthawi ino ya Adnenti ya caka ca 2006, pomwe paima nkhani yomwe ife a JCTR tipemha kuti Akhristu a mu Zambia asinke-sinkhepo ni nkhani ya utsogoleri wabwino kudzanso kuthetsa uphuphu, kubweletsa ciyanjano ndiponso kudalilika mu umoyo wa utsogoleri. Pomwe tisinkha-sinkha pa izi, tiyeni tikumbukire cikondi copambana ca Mulungu mu mau awa: “Monga Mulungu anakondera dziko lonse: kotero kuti anatipatsa mwana wake yekha kuti anthu onse okhulupirila mwa iye asataike koma akhale ndi moyo” (John 3:16).

Ndife othokoza Abambo Evaristo Chungu, a Pastoral Coordinator wa Lusaka Archdiocese, omwe anakonza mlozo wa kagawidwe ka mau mu Adventi. Tithokozanso asemino wa ku St. Dominic’s Major Seminary omwe anatembenuza mau awa.

Tidzakhala okondwa pakumva kwa inu za maganizo anu pa mlozo wa mauwa. Conde tipempha kuti mulembe maganizo anu pa pepala liri mkatimu ndi kutumidza mu kalata lodindidwa ndi inu. Zonena zanu zizatithandiza kukometsa za kutsogolo.

Ngati muzafuna ma pepala a mau awa tilembereni pa e-mail: jctr@jesuits.org.zm.

Ife aku JCTR tikufunirani mafuno abwino ndi cisangalala mu nthawi ya Adventi. Muli mu mapemphero athu ndipo tipemhpa kuti mutipempherereko. Chikhulupiriro cathu cibweletse cilungamo!

Zikomo, ndipo Mtendere wa Khristu!

Ndine,

Simson Mwale
Coordinator
JCTR Church’s Social Teaching Project

LA MULUNGU LOYAMBA MU ADVENTI CHAKA "C" 03 DECEMBER 2006

Mau oyamba: Yeremia 33:14–16
Mau achiwiri: 1 Thessalonika 3:12–4:2
Uthenga Wabwino: Luka 21:25–28, 34-36

CHILUNGAMO NDI KUKHULUPIRIRIKA PA UMOYO WA ANTHU

Matsiku ano, tiri kuona mabungwe kapena magulu a zamalonda m'dziko lathu kutsonkhanitsa zinthu zonse za pa malonda awo kuti aziwe momwe malonda awo alikuyendera. Pothera pa chaka, ndi nthawi yoonetsetsa ndi kustanda – standa pa zinchito zonse zinachitika mu chaka (evaluation). Koma kwa ife akhristu, nthawi ya Adiventi ndi nthawi yoyamba chaka china cha tsopano. Ndi nthawi yostinkha – stinkha pa umoyo wathu ndi Mulungu ndi anzanthu. Nthawi ino ya Adiventi ndi nthawi yokoma ya chaulele kwa onse okhulupiriri Khristu. Ifenso mu Zambia tiri okondwa ndipo othokoza pa mtendere unaoneka pa nthawi ya matsankho, koma tiri ndi chiyembekezero kuti atsogoleri athu adzakhala astogoleri ofuna kuthandiza pa kutumikira anthu.

Kale mwina tinalola atsogoleri oipa kukhala astogoleri athu chifukwa cha zichitidwe za uphuphu ndi kunama. Koma nthawi yafika tsopano yoti maganizo athu alole kwa Yesu Khritu ndi mkhalidwe wabwino wochokera mu uthenga wabwino. Andale onse apemphedwa kuti akhale achilungamo ndi okhulupiririka pa umoyo wao ndi umoyo wa anthu onse. Chilungamo kapena kukhulupiririka ndi kuchita chinthu choona koma chobvomerezedwa ngakhale palibe wina aliyense alikutipenyerera. Ichi chikhale chinthu chotithandiza pakati pa anthu maka – maka omwe tistogolera.

Mu mau oyamba lero, mneneri Yeremia sanabise mau ake. Monga Achewa amanenera: "Mneneri Yeremia sabisa mpeni pa nyama". Alutipempha kuti tikhale azimai ndi azibambo okhulupiririka. Tilore mitima yathu kukhala nyumba yoyera ya ku koma kwa Mulungu kuti tidzetse chilungamo m'dziko lathu.

Ino ndiyo nthawi yoti tilape machimo athu omangokonda kusamalira zathu zokha ndi kuiwalako za zofunikira za anthu onse. Ngati mu zimbumba, mabungwe, kapena m'midzi mwathu, tikhala otsamaganizilana; kuti aliyense azipezere zinthu zofunikira pa iye yekha kuti akhale ndi moyo, kodi umodzi wathu wochokera muchikhulupiriro chathu uli kuti? Chilungamo kapena kukhulupiririka mu umoyo kumapempha kuti tizindikire muthu aliyense kukhala m'modzi wa banja limodzi la anthu onse m'dziko lathu la Zambia, mopanda tsankho kulingana ndi mtundu, kapena umoyo wa zandare. Munthu wachilungamo kapena wokhulupiririka ndiokonzeka nthawi zonse kudzudzula njira zopondereza muthu wina chifukwa amaona kuti ndi iye yemwe aluponderezedwa. Iyi ndiyo tanthaudzo yomwe mpingo wathu pofuna kuphunzitsa za chilungamo, umati "kuyendera pamodzi" (solidarity). Iyi ndi nchito yathu akhristu maka-maka aja ali muutsogoleri, kukhala ndi chilakolako chofuna kuthandiza anthu otsauka.

Mu mau athu achiwiri, Paulo woyera, atiphunzitsa kuti chilungamo choona chimaonetsedwa mu umodzi wathu. Kusadziwa, sichifukwa chonveka cholepherera kuthandiza anthu omwe aluponderezedwa mu zimbumba zathu, m'midzi mwathu ndi m'dziko lathu. A Nelson Mandela omwe anali mtsogoleri wa dziko la South Afrika, anationetsa za umodzi wathu. Chimodzi – modzi, mwambi wina wa chi Chewa umati, "Kalikekha ndi ka nyama, tili tiwiri ndi tianthu".

Tinaona matsiku akale momwe anthu odwara kapena opwetekedwa ankalandirira thandizo. Nthawi zambiri, athu achuma kapena olemera ndi azandare akadwara, ankaperekedwa kuchipatala chapamwamba kunja kwa dziko lathu monga ku South Afrika (Ku Joni). Anthu osauka ankakhala chabe muzipatala zopanda mankhwala ndi zipangizo zofunikira ndi kulekeleledwa kuti afe. Mu malo amutali ngati mu midzi, anthu apakati mwina amayenda mistenga yaitali, ena ankafa po bereka

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

kapena pakuchira asanafike ku chipatala. Adotoro anali pa sitiraka. Omwe ankapeza bwino mwina anali aja ankapezeka muzandare.

A Papa Yohane Paulo Wachiwiri, analemba mu chaka cha 1989 kuti, “Umodzi ngati khalidwe, ndi kupirira kolimba pofuna kudzipereka pa kudzesta ubwino wa athu onse.” Mastiku ano, astogoleri afunika kudzesta umodzi wa mbali zosiyana-siyana kuti athandize kudzesta mtendere – “Zambia limodzi, Dziko limodzi.” (One Zambia, One Nation). Athandize kumanga umodzi osati kubweretsa mpatuko pakati pa athu chifukwa cha mtundu. Atsogoleri atithandize kuti tiyanjane wina ndi mzache. Tiphunzire kukolora zabwino zomwe tifetsa osati kungomadyerana matsuku pamutu; (Tidye nawo). Tiphunzire kugawane zinthu zonse. Tikamangoganizira za kuti tidye nawo chabe, khalidwe lathu lakugwira nchito ndi mphamvu limatha ndipo timakhala anthu aulesi ndi auphuphu (corruption).

Mu uthenga wathu wa lero, ambuye Yesu Khristu akutichenjedza kuti tisalole mitima yathu gugwa mumbuna ya zopanda pache kapena uchidakwa. Chifukwa zimenezi, zimatilekanitsa ife akhristu ndi udindo wathu wogwirizana naye Khristu kudzetsa ufumu wa Mulungu.

Zinthu zoterezi, zingathe kutigwetsa muzoipa monga kuchita zadama ndi tiana tochepa misinkho, kulowa mu magulu azi nchito za satana (satanic groups). Nthawi zina timagwiritsa nchito mphatso za bwino zamulungu mu njira zopanda pache monga uphuphu (corruption), uchidakwa ndi kusakhulupiririka mu ukwati. Koma mu uthenga walero, ambuye akutichenjedza kuti, “khalani matso” ndipo musatengedwe mitima ndi zinthu zoipa. Akhristu osakhwima amanyengedwa ndi zinthu zotere ndipo amapondereza ufulu wa athu.

Atsogoleri abwino, ali ngati dzitsulo za chilungamo. Pomwe tikukonzekera kubadwa kwa Mpulumutsi wathu, tiyeni timange umodzi wathu ndi chilungamo. Tingathe kutero mu njira zambiri pa umoyo wathu. Tikumbukire kuti ndife ana abanja limodzi, omwe afunika kuthandizana ndi kulemekezana.

MAFUNSO YOSINKHA SINKHA MUMA MBUMBA/MABUNGWE

- Kodi munthu kuti akhale mtsogoleri wabwino, afuniko khala munthu wotani?
- Kodi tingathandize bwanji atsogoleri athu m’dziko ndi mu mpingo kuti akhale achilungamo ndi okhulupiririka?
- Kodi tingathndize bwanji anyamata ndi atsikana athu kuti akhale atsogoleri abwino?

SEWERO

Pangani banja la anthu anai lomwe lili kusauka ndi kulira ndi njara, matenda ndi kusowekera kwa nyumba yabwino. Atate adandaula kuti palibe yemwe aonetsa chidwi chothandiza ngakhale aboma omwe. Munthu wina poona kubvutika kwa banjali, aganiza zothandiza, kubweretsa chakudya kuchokera ku nyumba yache, kupereka wodwala kuchipatala kuti akalandire thandizo ndi kumulipirira ndalama zofunikira. Banjali ndilodabwa chifukawa cha thandizo la munthuyu, kukhulupiririka ndi umodzi wake ndi banjali. Banjali lifotokozera munthuyu kuti mwina ndi bwino kuti aime pa matsankho, aukansela, kapena phungu la nyumba la malamulo kapena mtsogoleri wa dziko. “Ndinu wandare yemwe timafuna, yemwe amaganizira za anthu ena osati za iwo okha.”

MAPEMPHERO AMBUMBA

- Tipempherere atsogoleri aboma kuti abvomere kutsogoleredwe ndi Mulungu pa nchito yawo pa umoyo wa athu. *Ambuye mutimvere*
- Tipempherere atsogoleri a mpingo kuti atsogolere anthu amulungu mu choona ndi mu chikondi, kuwathandiza kutsata chitsanzo cha Yesu Khristu mu umoyo wao. *Ambuye mutimvere*
- Tepemphe kuti Mulungu akulitse chifundo mwa ife pa athu osauka ndi umodzi wathu maka-maka osowekera pakati pathu. *Ambuye mutimvere*

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

LA MULUNGU LA CHIWIRI MU ADVENTI CHAKA "C" 10 DECEMBER 2006

Mau oyamba: Baruki 5:1-9
Mau achiwiri: Filipi 1:3-6,8-11
Mthenga Wabwino Luka 3:1-6

CIPHUPHU NDI CHIMO

Tsiku lina pamene ndinali kuyendetsa galimoto mu mseu wa Independence Avenue, mu mzinda wa Lusaaka, ndinawona galimoto patsogolo panga, pagalimotoyi panali chipapala polembedwa mau akuti "Mulungu akuwonani!" Mu mtima mwanga dinaganiza kuti zimenezi nzokoma. Ndipo ndinakumbukila kuti matsiku ano, pamalamulo khumi a'mulungu tawonjezerapo malamulo awiri: lamulo la chikhumi ndi chimodzi (11): "ngati sunagwidwe sichimo ayi"; lamulo la chikhumi ndi chiwiri: "Ngati wagwidwa, nama bodza".

Tonse tinamvapo kupweteka kapena kuwawa kwa zipatso za Ziphuphu (corruption) mdziko lathu la Zambia, koma timaoneka ngati tikuvomekezana ndi Chilondachi (cancer) monga kuti ndi khalidwe lathu, kapena mwambo wa umoyo wathu muno mu Zambia. Mu Chibemba muli mau akuti "Kwindi abelesha ukwiba imbalala munganda ubushiku, alya nakasuba" (Ngati Kwindi adzolowela kuba nshaba usiku mnyumba, amadya ndi m'masana momwe). Koma tizikumbukila kuti Ziphuphu zipatsula/ziwononga chikondi.

M'mau oyamba alero, mneneri Baruki akutikumbutsa kuti tiyenera kugawana mphatso ya chimwemwe ndi anzathu potiitana kuti tivale chovala cha chilungamo. Mulungu akutipempha kuti tisatengeko mbali m'makhalidwe oipa a'Ziphuphu. Kodi tinganyadile bwanji mtendere wachilungamo ndi chimwemwe cheni cheni pamene tikana kutembenuke mitima ndikusiya chimo la Ziphuphu? Mu mau oyamba mulungu akutiuza kuti adza fotsera maphompho kuti ponse pasalale. Tiitanidwa kuti tisinthe makhalidwe oipa, ndipo tiyanjane ndi mulungu. Kodi kawili kawili sitimapanga maphiri atali atali ndi maphompho pakati pathu ndi mulungu, ndiponso pakati pathu ndi anzathu?

Timachita zimenezi pa ife tokha, ndiponso tizichita ngati mabungwe, pamene timatengako mbali mu za Ziphuphu mu khalidwe la "Mnyaule" (ndinyaule pamsana, nanenso ndizakunyaula). Kawili kawili timamva kuti azimai achitisidwa zopanda pache (sexual abuse) kuti awalonge ntchito. Ndipo ndi kangati pamene timamva kuti anthu azamalonda (investors) sasamala za umoyo wa antchito awo? Zonsezi zitchitika chifukwa chopanda kudziletsa pazilakolako za "nchekeleko." Kunena mwachilungamo, ngakhale ife ngati mpingo, kodi ndi chifukwa chani ana amu mabanja osauka kawili kawili sapeza malo mu masukulu athu abwino? Kodi kawili kawili sizimaoneka ngati kuti achuma angagule malo mumasukulu athu? Kupitila munjira ya Ziphuphu, kodi sitiletsa amphawi kuti nawonso akhale ndi maphunziro abwino? Kodi sitichita zimenezi modziwa ndi mwa ufulu?

Paulo woyera mu mau achiwiri akupempherera afilipi kuti akhale opanda cholakwa, ndipo akhalenso oyera. Akupemphera kuti chaulere cha mulungu chitsike pakati pakati pao. Tonsefe tifanizire a'filipi kukhala anthu ofuna zabwino. Tiyenera kuchitira umboni dziko lapansi, maka maka kwa anzathu pakukhala akhristu amachitidwe abwino. Koma mwatsoka lanji nthawi zambiri timafunafuna zotisangalatsa zimene sizilumikizana konse ndi umoyo wachikhristu.

Paulo akuthokoza afilipi pa chikondi chao ndiponso pa khalidwe lolandira alendo m'manyumba mwao. Tiyeni tikhale akhristu achilungamo maka maka potandiza amphawi. Mu Chitonga muli mau akuti "muchenge ngombe muchete tooni" (ukalonjeza munthu osauka kuti uzamphatsa ngombe, sagona tulo). Koma nthawi zambili tima pondeleza amphawi ndipo timawalonjeza malonjezo onama. Kodi sitimatengako mbali muzinthu zopanda ulemu ndi chilungamo mdzina la chitukuko?

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

Mu uthenga wabwino walero, tiona kudzama kwa chikondi cha mulungu, chikondi choposa makhalidwe athu oipa ndi machimo athu. Kupitila mwa Yohane m'batizi, mulungu akutidzuzula kuti titembenuke mitima ndikusintha makhalidwe athu. Yohane akutiitana kuti tiwongole umoyo wathu, tidzaze chigwa chilichonse, tichepetse zokhotakhota, ndipo tisalaze njira za maenje. Yohane akuti tisiye makhalidwe oipa aziphuphu ndipo titembenukile kwa mulungu. A'Bemba amati "ukwali nsoke takwafwile munthu", kutantauza kuti mumbumba/bungwe m'mene muli anthu amadzuzulana, ndipo amchenjezana. Chifukwa cha ichi palibe amene amafa.

Kulingana ndi mwambo umene unkha ukulira kulira muno mdziko lathu, mwambo wa "dyera"- Ulemelero kwa ena upezeka mu B.M.W: 'B' iimilira beer (mowa) umene timamwa; 'M' iimilra money (ndalama) zimene timafuna kupeza zifute zitani munjira iliyonse; 'W' iimilira women (azimai) amene timachita nawo zopanda pache. B.M.W itilonjeza chikondwelero chamsanga mnsanga ndipo cha padziko lapansi chabe. Koma ife akhristu tidziwa kuti chikondwerero cheni cheni ndi chosatha chipezeka mwa mulungu, ndiponso mukutumikira anzathu modzipereka ndi molungama. Munyengo ino ya Adventi Yohane M'batizi akutiitana kuti tisiye m'khalidwe waziphuphu ndipo tikonze chibwenzi chathu ndi mulungu, ndiponso ndi anzathu.

MAFUNSO YOSINKHA SINKHA MUMA MBUMBA/MABUNGWE

Kodi nthawi zina ndimakhala chete mu mbumba, mu mpingo, ndi kuntchito? Kodi ndi chifukwa chani ndimakhala chete?
Kodi ndimayankha bwanji anthu akandichenjeza pa za ziphuphu?
Kodi ndimalandira kawili kawili sacramenti ya chiyanjano? Ndikondamo chani mu sacramentiyi?

SEWERO

Khalani ndi kagulu monga Constituency Development Committee, m'mene munthu m'modzi ayanganila chuma cha anthu onse mbaliyo. Ndipo munthuyo akugwiritsa ncthito ndalama moipa, osasamala cholinga chake cha ndalamazo. Chifukwa cha ichi, bungwe lagwa, ndipo anthu ambiri abvutika ndipo asowa chitukuko. Anthu agulu la Anti Corruption Commission aitanidwa kubwera kuzamanga munthu uja, banja lake lionalera m'bale wao akuperekedwa kundende. Anthu onse akhumudwa ndipo atsimikiza kuti analikudziwa za ziphuphu za munthu uja koma sanachitepo chilichonse. "Tonse tili olakwa pamlandu wa munthu uja chifukwa tinakhala chete osamzduzula?

MAPEMPHERO AMBUMBA

- Tipemphere kwa mulungu kuti tisinthe makhalidwe aziphuphu, ndipo pakati pathu pakhale chikondi cheni cheni, kukonda anzathu ndikukonda mulungu, ndipo chikondichi chi chepetse maphiri m'mitima ndi muma mbumba mwathu. *Ambuye mutimvere, tikupemphani mutivomereze.*
- Tipempherere atsogoleri ampingo kuti adzilankhulilako onse anthu opendelezedwa, maka maka anthu amene achita zoipa kuti apeze umoyo wabwino. *Ambuye mutimvere, tikupemphani mutivomereze.*
- Tipempherere mbumba yathu, kuti tikhale olandira anthu m'manyumba mwathu, kutumikira anzathu kopanda kuyembekeza malipiro, tikhale gwero la chiyembekezo ndi chitontozo kwa onse amene akuvutika chifukwa cha ziphuphu. *Ambuye mutimvere, tikupemphani mutivomereze.*

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

LAMULUNGU LA CITATU MU ADVENTI CHAKA "C" 17 DECEMBER 2006

Cowerenga coyamba: Zefaniya 3:14-18
Cowerenga caciwiri: Filipo 4:4-7
Uthenga Wabwino: Luka 3: 10-18

KUFUNIKA KWA CIYANJANO

Mulungu amene tikhulupirira ndi Mulungu wopambana kusiyana kwathu ndi kulakhwa kwathu. Mulungu wathu afuna-funa ndi kuyembekeza aliyense wa ife ndi ciyembekezo cotilandira ndicikhululukiro. Mulungu afuna tonse kuti tiyanjane kotero kuti midzi yathu ndi dziko lathu liyanjane ndi Mulungu.

Mu cowerenga coyamba sabata loyamba la lero la Adventi, m'neneri Zefaniya asimikiza cikonzekero ca Mulungu kutilandira tonsefe ndi cikhululukiro: "*Kondwereni, sangalalani ndi mitima yanu, ana a Yerusalemu*. *Ambuye abweza cilango canu.*" Mkati mwa caka ca cipembedzo ca 2006, mwina tinayambana ndi anzathu, ndi anansi athu, atsogoleri a ndale kapena ndi zipani zina. Tsono pomwe tithamangira ku Khrismas, tiitanidwa kuti tikonze ma ubale athu osweka. Tipemphedwa kukonza kusiyana kwathu.

Mkulu wa mpingo wochuka kwambiri mu South Afrika, Bishop Desmont Tutu, nthawi ina ananena za kufunika kwa kuyanjana ndi anzathu mu mau ocititsa cidwi: "*Popanda ciyanjano, palibe tsogolo*." Inde, inu ndi ine tidziwa kuti ciyanjano ndi gwero la kumanganso midzi yathu ndi dziko lathu la Zambia.

Atsogoleri athu, motsogoleledwa ndi maphunziro a cikhulupiriro ayenera kutiyika tonsefe mu njira ya ciyanjano kudzera mu msinthu wa maganizo ao ndi zicitidwe zao kwa anzao. Monga Paulo Woyera atiphunzitsira mu cowerenga caciwiri mu kalata yolembera Afilipo, cifuniro ca munthu aliyense ndi bata ndi mtendere kuti udze pakati pathu. Iyi inali pemphero la Paulo lofuna kuti Mulungu akudze mtendere wa Afilipo.

Komanso sitingathe kupeza mtendere woona ndi cimwemwe coona ngati sitiyanjana. Atsogoleri athu a ndale afunika kuonetsa kwa ife tonse kuti afuna kutipatsa mphaso ya Khrismas pokhululukirana pomwe ndi kofunika kutero. Kucokera pa nthawi ya kampeni kufikira masankho kunali kuponyelani mau onyodola, kunenezana, ndi kuopsezana mokalipirana. Koma tsopano tifunika kupita patsogolo ngati dziko limodzi – "One Zambia, One Nation" pokudza ciyanjano pa mbali zonse.

Kuitanidwa uku kuti tiyanjane kufunika kusinthika kwa mitima, maganizo ndi kakhalilidwe. Kusasamala za ciyanjano ndi anzathu kuyelekezera kuzula maziko ya "ulamulira wabwino." Macimo ena monga kukondera mtundu wako ndi kusabvomereza za ndale afunika kulapidwa. Ino sinthawi yolatana zala kapena kudzudzulana.

"Anyani sasekana cikudu" Mwambi uyu utithandiza kuti tisasekane zolakwa zathu cifukwa tonse tinalakwapo mu njira ina nthawi ina. Nthawi ya ciyanjano yafika. Ndi nthawi yocita kufuna kwa Khristu.

Mu nthawi ya Adventi, tipemhedwa kuyendera mwa njira ya padera anthu osauka ndi wosowekera pakati pathu. Tifunika kugawana nao zomwe tili nazo anthu osowekera awa mu midzi mwathu. Ndi zoonadi, tiri ndi udindo waukulu wothandiza aja anasausidwa cifukwa ca uphuphu pakati pathu
Mu uthenga wabwino wa lero, Yohane Mbatizi afotokozera azimai ndi azibambo ogwira nchito mu ma ofesi a boma kukhala okhulupirika. Akuti agwire nchito yao mopambana ndi moona. Iye akucula makamaka osonkhetsa msonkho ndi asilikali. Koma mau ake akudza onse omwe ali ndi maudindo. Kodi tigwilitsa nchito motani maudindo awa? Inde ndicokalipitsa kumva kuti anyanchito ena akhala

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

mopitililira zomwe apeza cifukwa ca kutengako mbali mu zonyenga ndi zaciphuphu. Ndi kotheka bwanji kuti azikhala ndi nyumba zokula tere, kumayendetsa magalimoto odula tero, kubvala zobvala zokongola tero, ndi kupanga maulendo okoma tero? Kunena coona, sangathe kukhala tero ndi malipiro a boma anthawi zonse kapena malipiro a pa malonda!

Cokwiyitsanso, tidziwa kuti anyanchito ena agwiritsa ulamuliro wao pozunza anthu opanda dzina mu Zambia. Nthawi zina acita izi kwa aja anathawa nkhondo kwao – anthu obvutika kale ndi mazunzo a ku maiko akwao – azunzika mopanda cifundo ndi akulu a boma onyenga.. Ma refujizi ofuna kuyamba tu mabizinesi mu Zambia ayenera kuonetsa bank statement ya 25,000 US dollars ndipo ayenera kulipira K2 million kuti okonzetse citupa cocitira malonda. Ndipo ma refujizi ofuna cilolezo ca maphunziro ayenera kulipira K500,000.

Ca kumbuyo uko ndinamva za nkhani ya umoyo wa mu refuji wina wa zaka 14 wocokera ku Congo, mwana wa sukulu wokhala mu komboni ina ku Lusaka ndi amai ake odwala kwambiri. Mtsikana uyo anampeza wa Immmigration akugulitsa malonda ake pa msika. Anamgwira pokhala kuti analibe citupa ca malonda ndi nchito. Anamponya m'ndende kwa sabata limodzi. Anakhala osapita ku sukulu ndiponso kunalibe othandiza amai ake odwala. Komanso analibe njira yopezera 25,000 US dollars ndi K2 million kuti akhale ndi citupa za malonda ndi cililezo ca sukulu.

Aliyense, pamodzi ndi oyanganira malamulo, ayenera kumva mau ya Yohane Mbatizi ndi kukhala okhulupilika ndi kukhala ndi mtima wa cifundo kwa anthu. Ulamuliro wozikhuza wozionetsa ndi utsogoleri wa ciphuphu siudzatithandiza kukula ndi kutukuka mu Zambia. Pa nthawi ino ya Adventi, tonse tiitanidwa kulapa macimo athu. Tifunika kuyanjana ndi Mulungu ndi anzathu. Kulingana ndi mfundo zomwe tipanga, anthu adzaziwa kuti tiri a Khristu kapena ai.

MAFUNSO YOSINKHA SINKHA MUMA MBUMBA/MABUNGWE

- Kodi ndi ciani cimatitsa kuti anthu acite za ciphuphu mu midzi/komboni ngakhale mu mpingo wathu?
- Ngati ndine mtsogleri, kodi ndigwirtsa ulamuliro wanga moopseza anzanga?
- Ndi zobvuta zotani zomve ndipeza pobweretsa ciyanjano pakati pathu, komanso kodi ndicitapo zotani kubweretsa ciyanjano?

SEWERO

Pakhale atsogoleri andale awiri oyimilira zipani za ndale ziwiri. Mtsogoleri umodzi akhale wolephera pa masankho ndipo wina akhale ocita bwino. Onse awiri apepese pa maso pa anthu cifukwa conyozana ndi kubweretsa tsankho la mtundu wao mu ckhalidwe cao. Atayanjana, akumbatirane. Kutsatira apo, m'modzi ayambe nyimbo ya ciyanjano, apo ena ataimikiza zipepala zolembedwa: "*Popanda ciyanjano palibe tsogolo."*

MAPEMPHERO AMBUMBA

- Tipempha Ambuye kuti mutipatse luntha lobvomera kulakhwa kwathu komwe tinaonetsa pokalipira anzathu mu mau ndi m'macitidwe. *Ambuye mutimvere, tikupemphani mutivomereze.*
- Tipempha Ambuye kuti mutikhululukire pa nthawi zambiri zomwe tinabweretsa kusiyana mu mbumba zathu cifukwa ca zifuniro zathu. *Ambuye mutimvere, tikupemphani mutivomereze.*
- Tipempha, Ambuye, kuti mutipatse mphamvu zokambilako opondelezedwa mu ma mumba mwathu. *Ambuye mutimvere, tikupemphani mutivomereze.*

LA MULUNGU LA CINAI MU ADVENTI 24 DECEMBER 2006
CHAKA C

Mau oyamba: Micah 5:1-4
Mau aciwiri: Hebrews 10:5-10
Uthenga Wabwino: Luke 1:39-44

UTSOGOLERI WA NCITO

Lero ndilamulungu lacinai la advent pafupi-fupi ndi nthawi ya kubadwa kwa mpulumusi, mfumu yamtendere Yesu Khristu. Masauzande awiri omwe apitawa ndiye nthawi yomwe Ambuye Yesu anabadwa pakati pathu nakhala ngati munthu wozicepesa padziko lino lathu. Mwaici, tizindikira kuti nthawi yonse yamasiku athu, tiri nao mu umoyo wathu ndi abale onse. Cikondwelero ca Khisimisi sicikondwelero cabe cakale caku dziko lina lakutali koma ndi cikumbutso kuti Yesu Khristu tiri naye pakati pathu mu dziko lino lathu la Zambia, mu caka ca 2006.

M'profeti Mika mu cowerenga coyamba atikumbutsa kuti kubwera kwa mpulumusi azacokera mu banja la mfumu Davide ndipo azakhala wozicepesa. Mwaici, mutsogoleri wabwino afunika kukhala munthu wozicepesa. Kuzicepesa kuli ngati mai wa makhalidwe onse abwino. Mutsogoleri wozicepesa amazindikira zomwe angathe kucita ndi zomwe sangathe kukwanilitsa.

M' nthawi ya m'profeti Mika atsogoleri ambiri-mbiri anali cabe ndi mtima wofuna kupata cuma ndi mphamvu mu utsogoleri wao. Anaiwala amphawi namanzunza anthu ao. Dziko lonse la Yerusalemu linakhala cabe ndi atsogoleri oterewa. Koma m'profeti mika alankhula kuti Mulungu azacita cotheka kutuma mutsogoleri wabwino yemwe azakhala mfumu ya mtendere amene aza weta nkhosa zake.

Mziko lino la Zambia naifenso takhala nawo azitsogoleri okonda cabe cuma ndi mphamvu za utsogoleri. Atsogoleri amenewa ndiwo omwe akhala pakati kuletesa kusagwilizana pa mitundu yathu. M'malo momwe ticokera, timawawona anthu oterewa ofuna kuti zinthu zonse zikhale m'manja ao. Ndipo takhala ndi bvuto pakanthawi poona kuti kawiri-kawiri anthu ali ocepa afuna kutsogolera anthu oculuka mowonongeka. Zimenezi zapangitsa kuti tikhale anthu olephera kucita zitukuko patekha ku midzi kwathu kapena m'dziko lomwe.

Tsono ncifukwa cake ngakhale kuti mau a m'profeti analankhulidwa kale-kale koma tsopano afunikanso kutikhudza. Mprofeti m'meneyu afuna kuti utsogoleri wathu ufane-fane ndi Yesu Khristu. Modzicepesa kwake, Yesu abwera kuti azatipulumutse naleta khosa zake pamodzi nakhala mfumu yamtendere.

Mucowerenga caciwiri cocoka mu Aheberi, ncito zampulumutsi zisimikizidwa pakutero kuti iye azacita zomwe Mulungu akufuna: "ndinabwera kuti ndicite kufuna kwanu." Atsogoleri abwino afunikanso kukhala anthu owopa Mulungu. Afunika kutumikira anthu ao popanda kudyera anzao masuku pamutu. Motero amafunika kukhala ozipeleka nthawi zonse osati kukhala ndimaganizo a azitsogoleri ambiri omwe maganizo ao ndi akuti tidye nao.

Coipanso ncakuti, azitsogoleri amenewa akhala ozikudza nakhala wanthota motero kuti alibe nthawi yomverako maganizo ya anthu omwe anawasankha. Cacikulu kwa iwo ndi cuma ndimaganizo ao okha. Amaiwala mwambi wa acewa yemwe umati "ukakwera m'mtengo osatukwana ali pansi cifukwa ukagwa kulibe azakutola." Iyi phunziro iwophyeza atsogoleri kuti akakwezedwa pa mwamba wamtengo wa udindo womwe ali nao, safunika kutukwana anthu omwe ali pansi. Mtsogoleri owona alemekeza anthu ake ndiponso akhala ndi cikhulupiriro mwa iwo. A Wemba nao amati: "ubufumu bucindika abene" kunena kuti atsogoleri omwe azilemekeza, anthunso azawalemekeza.

M'mthenga walero wa Luka, Mulungu alemekeza mfumu yacicepele lochedwa kuti Maria. Pakuvomera kucita kufuna kwa Mulungu, mai m'meneyu anagwapo pancito yotipulumutsa ife.

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

Cimeneci ndico cisanzo ca utsogoleri weni-weni wa mai m'meneyu yemwe anabweletsa Yesu pakati pathu.

Tsono pamene tiri kufendera pafupi ndi nthawi ya khisimisi tifunika kuthokoza Mulungu ndi Amai Maria omwe anabvomera kukhala mai wa Yesu Khristu. Mozicepesa kwao, anabvomera kukhala mai wa mpulumutsi ndiponso anabvomera kudzetsa cipulumutso. Tsopano popeza kuti Mulungu mu ncito yace yodzetsa cipulumutso anagwiritsa ncito munthu wa cizimai, ncifukwa ciani nthawi zino timafuna kusautsa azimai athu pakuwa pondeledza, kuwalekelera, ndi kuwanyoza?

Ife pokhala ngati akhristu tifunika kupasa azimai athu danga loti nao akhaleko azitsogoleri mu ncito zapamwamba m'midzi mwathu. Mulungu yemwe anafuna kusewenzetsa azimai m'ncito ya cipulumutso ndiponso tiziwa bwino-bwino kuti anthu amenewa ndiwo amene amanga midzi yathu. Yesu anabadwa pakati pathu nakhala pamodzi ndi makolo ace Yosefe ndi Maria. Ngati tamva Uthenga Wabwino wocokera pakamwa pa Yesu tifunika kuganizilapo kuti mwina uthengawu unacokera kwa makolo ace Yosefe ndi Maria.

Tsono paici, makolo afunika kuzindikira kuti banja liri lonse ndilo sukulu la utsogoleri wabwino. Ana angathe kuphunzira zambiri kucokera m'mabanja athu nkhani ya utsogoleri wabwino namagwapo kuthandiza anzao. Ngakhale kuti ino ndi nthawi ya umphawi, makolo sayembekezedwa kusiya ncito yao yolera ana namaganiza cabe pa zacuma. Mpatso yayikulu yomwe makolo angapatse ana ao pa nthwi iyi ya Khisimisi ndikupeza mpata wokhala limodzi nao. Cimeneci citha kudzetsa mphoto ikulu ku ana ndiponso dziko lonse.

Tifunika kugwapo pomanga "One Zambia, One Nation" (Dziko limodzi, Mtundu umodzi) popereka zisanzo zabwino ku ana athu. Imeneyi nkukhala njira imodzi yocoselamo zicitidwe zonyansa monga kusagwirizana kwa mitundu ndi ziphuphu. Atsogoleri abwino amamva ndipo atha kugwira ncito zao ngakhale kuti iwo ndi makolo amabanja, kapena akulu a boma ndi aza malonda, kapena osankhidwa andale.

MAFUNSO YOSINKHA SINKHA MUMA MBUMBA/MABUNGWE

- Tculani atsogoleri abwino omwe zincito zao taziwona mu dziko lathu kapena mu calici? Kodi macitidwe ao ngotani ku anthu?
- kodi ndine mtsogoleri wabwino amene ali ndi anthu omwe ikapo mutu pa ine? Kodi utsogoleri wanga ndi wankhanza, mwacisanzo mubanja?
- Ndi njira ziti zomwe ndingasewenzetse kulesa cipongwe, kusula ndi kuzingwitsa acizimai m'midzi kapena m'macalici athu kuti iwo akhaleko azitsogoleri?

SEWERO

Khalani ndi anthu awiri, mwamuna ndi mukazi ndipo muwaleke kuti agwebane pa mpando waku mbumba yanu. Alekeni alankhule zomwe ali nazo ndipo anthu ena azilemba zinthu zomwe mufuna m'mutsogoleri wabwino. Mwacisanzo mutsogoleri wokhulupirika, wozicepesa, wanzeru, wogwira ncito bwino ndipo wozipereka ku anthu onse. Pa nthawi iyi mzimai azakhala pamwamba pamasankho. Muzibambo wogonjetsedwa ndi anthu onse nthawi ino agwepo kumthokoza mzimai iyu!

MAPEMPHERO AMBUMBA

- Tipemphe kuti Mulungu atipatse atsogoleri olungama omwe azatha kutisewenzera mofatsa ndi mwacikondi. *Ambuye mutimvere. Tikupemphani mutivomeleze.*
- Tipemhe kuti Mulungu atipatse caulere pozindikira ncito zomwe azimai athu akhala akugwira m'midzi mwathu. *Ambuye mutimvere. Tikupemphani mutivomeleze.*
- Tipemphe mphamvu ya Mzimu Woyera kuti iwalitse mabanja athu kuti akhale sukulu labwino la umboni wacikhristu ndinso utsogoleri. *Ambuye mutimvere. Tikupemphani mutivomeleze.*